KATEKISIMU WA MBIRI YA BAIBULO
NKHANI ZA M'BAIBULO ZA M'CHIPANGANO CHAKALE

(kuyamba kwa Saulo kufikira kubwerera ku ukapolo)

Oyamba kumene kuphunzira (Kalasi Yoyamba)
Buku Lachiwiri la Atatu

Lalembedwa ndi **Rev C.Hanko**
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

January 2011 edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Katekisimu wa mbiri ya M'baibulo- Nkhani za M'baibulo za chipangano chakale
(kuyamba pa Saulo mpaka kubwerera kuchokera ku ukapolo)
(Oyamba kumene Kuphunzira- Buku lachiwiri la atatu)

Lalembedwa ndi **Rev C.Hanko**
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene anatanthauzira ndi Rev C, Hanko eni ake ndi a Prostestant Reformed Churches of America
Buku ili lakonzedwanso ndi Rev. J.J. Lim mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

MAU A MLEMBI

Buku ili ndi lachiwiri mwa mabuku atatu lomwe limafotokoza za mbiri ya Baibulo mwa nkhani kwa ana azaka za pakati pa zisanu ndi chimodzi mpaka zisanu ndi zitatu za kubadwa.Buku limeneri likufotokoza za mbiri kuyambira pa ulamulilo wa Saulo kufkira nthawi imene Ayuda anabwerera kuchokera ku ukapolo. Mphunzitsi adziwe kuti ayenera kuphunzitsa mfundo imodzi kapena ziwiri zokha zimene akhoza kuziika mu phunziro lililonse,osati kulowa mkati kwambiri. Mphunzitsi adziwe mmene angachitire potambasula mfundozi, ndikuikamu mfundo zothandizira kuti zokambirana zake zimveke bwino m'kalasi.

Ndikupempha Mulungu kuti atithandize kukwaniritsa lonjezo lake mwa ife kuti Iye akhale Mulungu wathu komanso Mulungu wa muyaya kwa mibadomibado. Ili ndi pemphero lathu ndipo mdalitso wa chokhumba chathu.

-Rev C.Hanko

MAU A MKONZI

Kugwiritsa ntchito katekisimu potsogolera ana m'tchalichi ndi njira yabwino ndipo yoyenera nthawi yabwino. Katekisimu wolumikizana wa mbiri ya baibuloyu yemwe ife tikugwiritsa ntchito anapangidwa ndi a Protestant Reformed Church (Ngakhale kuti tikugwiritsa ntchito mitu yosiyana) Cholinga cha Katekisimuyu ndi kuthandiza ana kuti azame ndi mfundo ngakhale mbiri ya baibulo, zimene zingawathandize kuima ndi chiphunzitso chokhazikika monga cha Katekisimu Wachidule wa Westminister. Tankonza monse moyeneraa ndi kusintha ena mwa mafunso chicholinga chokonza zolakwika kapena kuwonjezera mphamvu za kamvekedwe kuti ogwiritsa ntchito azimvetsa bwino.

Ngati mwana wanu ali ndikuthekera koloweza mwansanga m'sabata imodzi mafunso onse khumi ndi mavesi oloweza, ndikulimbikitsani kuti mumuuzenso aloweze mwaukaswiri mafunso ena kuchokera mu Katekisimu wa ana ang'onoang'ono. Chiyambi cha Katekisimu wa Westminister chidzaphunzitsidwa pakutha pa mabuku atatu a Katekisimu wa mbiri ya Baibulo (Kalasi yoyamba)

Buku lothandizira buku ili latsindikizidwa. Makolo akulimbikitsidwa kuthandiza ana awo kugwiritsa bwino mabaukuwa pawonjezera kuwathandiza kuloweza mayankho khumu pa sabata iliyonse. Aphunzitsi a kutchalitchi ntchito yawo ndi kuthandizira basi koma udindo waukulu uli ndi makolo maka abambo. Ana akafika m'kalasi, aphunzitsi awo adzangowapatsa maphunziro ochepa okha ofunika kuganiza, ndipo adzangodutsa chabe maphunziro aja ndi ophunzira aliyense pomuyetsa iye zomwe waloweza. Tikupempha Mulungu atidalitse ife ndi mphamvu zathu zochepazi kuti tiwalangize ana athu mu njira ya Ambuye.

-Rev. J.J. Lim

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 1
SAULO
1 Samueli 8-15, 28,31

1.Kodi ndi chifukwa chiani a Israeli anafuna mfumu?
Amafuna afanane ndi mafuko ena. (1 Samueli 8:4-5)

2.Kodi Mulungu anawapatsa mfumu?
Inde, anawapatsa Sauli wa fuko la Benjamini. (1 Samueli 9:16-17; 10:1)

3.Kodi Sauli anali mfumu yabwino?
Ayi, anali wochimwa kwambiri. (1 Samueli 15:10-11)

4.Kodi Sauli anaonetsa bwanji kuchimwa kwake?
Sanamvere malamulo a Mulungu. (1 Samueli 13:7-14; 15:1-9)

5.Kodi Mulungu analanga bwanji Sauli?
Anamulanda ufumu kuchokera kwa iye. (1 Samueli 15:22-30)

6.Kodi Mulungu anayankhulanso ndi Sauli zitapita izi?
Ayi, Mulungu sanayankhulenso ndi iye. (1 Samueli 28:6,15)

7.Kodi Sauli anayeseranso kufuna thandizo kwa Mulungu?
Inde, asanakamenye nkhondo ndi a Filisti. (1 Samueli 28:3-6)

8.Kodi Sauli anapita kuti chifukwa choti Mulungu sanafune kumuyankhula iye?
Anapita kwa owombeza wina usiku. (1 Samueli 28:7-8)

9.Ndiuthenga wanji umene Sauli anapeza?
Anauzidwa kuti iye akaphedwa. (1 Samueli 28:19-20)

10.Kodi Sauli anafa bwanji?
Anadzipha yekha ku nkhondo. (1 Samueli 31:1-5)

VESI LOLOWEZA:
"Pakuti Yehova adziwa mayendedwe a olungama koma mayendedwe a oipa adzatayika" (Masalimo 1:6)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 2
DAVIDE ADZOZEDWA NGATI MFUMU
1 Samueli 16 – 28

1.Kodi Samueli anamudzoza ndani mmwalo mwa Sauli?
Davide yemwe anali wa fuko la Yuda. (1 Samueli 16:11-13)

2.Kodi Davide amapanga chiani pamene anali mnyamata?
Anali oweta nkhosa za makolo ake. (1 Samuel 16:11,19; onaninso 17:15,20)

3.Kodi Mulungu anali ndi Davide nthawi imeneyi?
Inde, Mulungu anamuteteza ku mkango ndi chimbalangondo. (1 Samueli 17:34-37)

4.Kodi amene ananyoza a nkhondo a Israeli ndi ndani?
Chimphona, Goliati. (1 Samueli 17:4, 8-10,26)

5.Kodi Davide anapanga chiani kwa Goliati?
Anamupha iye ndi legeni. (1 Samueli 17:47-50)

6.Kodi Saulo anasangalala kuti Davide adapha Goliati?
Ayi, anachita nsanje ndi Davide. (1 Samueli 18:7-9)

7.N'chifukwa chiani anachita nsanje ndi Davide?
Anadziwa kuti Mulungu ampanga Davide kukhala mfumu. (1 Samueli 16:1-4; onaninso 20:31)

8.Kodi Sauli anayetsera motani kufuna kupha Davide?
Anamusaka iye ndi asilikali ake. (1 Samueli 23:7-8)

9.Kodi Davide anabisala kuti?
Anabisala kumphanga ku mapiri. (1 Samueli 24:1-8)

10.Kodi Saulo anatha kumupha Davide?
Ayi, pakuti Mulungu anamusamalira nthawi zonse. (1 Samueli 27:4; onaninso 28:16-17)

VESI LOLOWEZA :
"Inde, ndingakhale ndiyenda m'chigwa cha mthunzi wa imfa, Sindidzaopa choipa; pakuti Inu muli ndi ine; " (Masalimo 23:4)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 3
DAVIDE NGATI MFUMU
2 Samueli 2 -12

1.Analowa ufumu Sauli atafa ndi ndani?
Davide, amene amaopa Mulungu. (2 Samueli 2:1-4)

2.Kodi Davide amakhala kuti ?
Amakhala ku Yerusalemu. (2 Samueli 5:6-7, 9)

3.Kodi Davide anabweretsa chiani ku Yerusalemu?
Likasa la Mulungu. (2 Samueli 6:12, 15-17)

4. Kodi Davide anakonza kuti amange chiani ku Yerusalemu?
Kachisi okongola kwambiri wa Mulungu. (2 Samueli 7:1-5; onaninso 1 Mafumu 8:17)

5.Kodi Davide anamanga kachisiyu?
Ayi, Mulungu anamuuza kuti mwana wake Solomoni ndiye adzamange kacisiyu. (2 Samueli 7:11-13; onaninso 1 Mafumu 8:18-19)

6.Tchulani tchimo lalikulu lomwe Davide analichita.
Anatenga mkazi wamwini wake. (2 Samueli 11:2-5)

7.Kodi Davide anafuna kubisa tchimo lolanda mkazi wa mwini wake motani?
Anamupha mwamunayo pomuika patsogolo pa nkhondo. (2 Samueli 11:14-17)

8.Kodi Davide anakhuzika ndi tchimo limeneri?
Inde, koma kufikira Mulungu anatumiza mneneri Nathani kwa iye.
(2 Samueli 12:1-13; Masalimo 32; Masalimo 51)

9.Kodi Mulungu anasonyeza bwanji kuipidwa kwake ndi Davide?
Anabweretsa matenda kwa mwana wake ndipo anamwalira. (2 Samueli 12:14-23)

10.Kodi Mulungu anamulanga Davide mwa njira ina?
Inde, Mulungu anabweretsa mavuto ambiri pa banja lake. (2 Samueli 12:10-12)

VESI LOLOWEZA:
"Wodala munthuyo wokhululukidwa tchimo lake; wokwiriridwa choipa chache. (Masalimo 32:1)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 4
TCHIMO LA ABISALOMU
2 Samueli 15-19

1.Kodi Abisalomu anali ndani?
Anali mwana wa Davide. (2 Samueli 3:2-3)

2.Ndi tchimo lanji limene Abisalomu adachita?
Anafuna kulanda ufumu wa bambo ake. (2 Samueli 15: 1-12)

3.Chimenechi chinali cholakwika kwa Abisalomu chifukwa chiani?
Chifukwa Mulungu ndiye anampatsa ufumu Davide. (2 Samueli 5:3; onaninso 1 Samueli 24:10)

4.Kodi anthu anafuna Abisalomu kuti akhale mfumu yao?
Inde, anthu ambiri anamukonda iye. (2 Samueli 15:13)

5.Kodi Davide anafuna kumenyana naye mwana wake Abisalomu?
Ayi, anathawa kuchoka ku Yerusalemu. (2 Samueli 15:14)

6.Kodi Davide anathawa yekha?
Ayi, ndi asilikali a nkhondo omwe anapita naye. (2 Samueli 15:15-18)

7.Kodi Abisalomu anamutsatira Davide?
Inde, anapita ndi asilikali kuti akammenye iye. (2 Samueli 17:1, 24-26)

8.Chinachitika ndichiani pakati pa asilikali a Davide ndi a Abisalomu?
Abisalomu anakodwa mutu wake mziyangoyango za mitengo. (2 Samueli 18: 9-10)

9. Kodi nkhondo inatha bwanji?
Abisalomu anaphedwa. (2 Samueli 18:14-17)

10.Kodi Davide anabwerera ku Yerusalemu?
Inde, anakhalanso mfumu ngati kale. (2 Samueli 19:14-15)

VESI LOLOWEZA:
"Mulungu ndiye pothawirapo pathu ndi mphamvu yathu,thandizo lopezekeratu m'masautso" (Masalimo 46:1)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 5
SOLOMONI
1 Mafumu 1 – 11

1.Kodi anakhala mfumu ndani Davide atamwalira?
Solomoni, monga m'mene Davide ananenera. (1 Mafumu 1:17, 34-35, 39; onaninso 2:1-2, 12)

2.Kodi Solomoni anafunsa chiani kwa Mulungu?
Nzeru kuti alamulire bwino anthu. (1 Mafumu 3:8-12)

3.Kodi Mulungu anampatsa Solomoni nzeru?
Inde, ndipo Mulungu anampatsanso chuma ndi ulemelelo. (1 Mafumu 3:13; 4:29-30)

4.Kodi Solomoni anaonetsa nthawi yanji nzeru zake?
Pamene amayi awiri amalimbirana mwana m'modzi. (1 Mafumu 3:16 -28)

5.Kodi Solomoni anamanga chiani?
Kachisi wamkulu ndi okongola. (1 Mafumu 6:1-10)

6. Ndichifukwa chiani mfumu yaikazi ya ku Seba inafika kwa Solomoni?
Kuti akaone ulemerero umene Mulungu anampatsa. (1 Mafumu 10:1, 4-9)

7.Kodi Solomoni anachita tchimo lotani?
Anakwatira akazi ambiri achikunja. (1 Mafumu 11:1-4)

8.Kodi akazi amenewa anapangitsa kuti iye achimwilibe?
Inde, anampangitsa kuti ayambe kupembeza mafano. (1 Mafumu 11:7-8)

9.Kodi Mulungu anaonetsa bwanji kuti zimenezi zanamuipira?
Mulungu anatenga gawo limodzi la ufumu wake kuchokera kwa mwana wake.
(1 Mafumu 11:9-13)

10.Kodi Solomoni analapa?
Analapa ndithu; ndipo analemba buku la Mlaliki ku ukalamba wake. (Mlaliki 12:13-14)

VESI LOLOWEZA:
" Kuopa Yehova ndiko chiyambi cha kudziwa"(Miyambo 1:7)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 6
REHOBOAMU, MFUMU YA AYUDA
1 Mafumu 11 - 14

1.Kodi analowa ufumu pa mbuyo pa Solomoni anali ndani?
Mwana wake Rehoboamu. (1 Mafumu 11:43 - 12:1)

2.Kodi anthu anamufunsa Rehoboamu kuti awachitire chiani?
Anamufunsa kuti atsitse misonkho yao. (1 Mafumu 12:3-4)

3.Kodi Rehoboamu anavomera zomwe anthu amafunazo?
Ayi, anawayankha mokalipa ndipo anawauza kuti aonjezera misonkho yao.
(1 Mafumu 12:12- 14)

4.Kodi anthu anamuukira bwanji Rohaboamu?
Mafuko khumi anampanga Yeroboamu mfumu yao. (1 Mafumu 12:20)

5.Kodi ichi chinali choyenera kuti anthu achichite?
Ayi, Mulungu anampanga Rehoboamu mfumu yao. (1 Mafumu 12:1; onaninso 1 Samueli 24:10)

6.Kodi mafuko khumi amenewa ndi ati?
Fuko la Israeli, kapena fuko la kumpoto. (1 Mafumu 12: 19-20)

7.Ndimafuko angati amene anakhala ndi Rehoboamu?
Awiri, Yuda ndi Benjamini. (1 Mafumu 12:21)

8.Kodi mafuko awiriwa amatchedwa chiani?
Mafuko a Yuda kapena mafuko a kummwera. (1 Mafumu 12:23, 27)

9.Kodi Rehoboamu anatumikira Mulungu nthawi zonse?
Ayi, iye ndi anthu anasiya kutsatira Mulungu. (1 Mafumu 14:21-24)

10.Kodi Mulungu anamulanga bwanji iye?
Mulungu anatuma mfumu ya ku Egypt kuti alimbane naye. (1 Mafumu 14:25-26)

VESI LOLOWEZA:
" Yehova chifundo chanu chikhale pa ife, Monga takuyembekezeni Inu" (Masalimo 33:22)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 7
YEROBOAMU , MFUMU YA ISRAELI
1 Mafumu 12 -14

1.Kodi Yeroboamu anali mfumu yabwino?
Ayi, anayambitsa Israeli kupembeza ana ang'ombe agolidi. (1 Mafumu 12:28)

2.N'chifukwa chiani Yerobiamu anapanga ng'ombe za golidi?
Samafuna kuti anthu azipita ku kachisi ku Yerusalemu. (1 Mafumu 12:26-30)

3.Ndi ndani amene anatsutsa za guwa la nsembe limene Yeroboamu anapanga?
Mneneri wochekera ku Yuda. (1 Mafumu 13:1-2)

4.Chinachitika ndi chiani pamene mneneriyu ananena motsutsana ndi guwa?
Guwa linang'ambika m'ziduswaziduswa. (1 Mafumu 13:2-5)

5.Chinachitika ndi chiani ndi mneneri uja panjira popita kwao?
Anaphedwa ndi mkango. (1 Mafumu 13:24)

6.N'chifukwa chiani mneneri anaphedwa ndi mkango?
Chifukwa choti sanapite ku Yuda mwansanga monga mmene Mulungu anamuuzira.
(1 Mafumu 13:7-9, onaninso v 11-19, 25-26)

7.N'chifukwa chiani mneneri uja sanatsatira zomwe Mulungu anamuuza?
Chifukwa wina anamunamiza kuti Yehova wayankhula ndipo anamunamiza iye kuti asapite.
(1 Mafumu 13: 18 mpaka kutsogolo)

8.Kodi Mulungu anamulanga bwanji Yeroboamu?
Mulungu anadwalitsa mwana wake wamwamuna. (1 Mafumu 13:33-14:1)

9.Kodi mkazi wa Yeroboamu anateteza bwanji moyo wa mwana wake?
Anapita kwa Ahiya mneneri wa Mulungu. (1 Mafumu 14:2-5)

10.Kodi Ahiya anamuuza chiani mkazi wa Yeroboamu?
Anamuuza kuti mwana wake afa ndithu. (1 Mafumu 14:6, 12-13)

VESI LOLOWEZA:
" Pakuti Inu sindinu Mulungu wakukondwera nacho choipa." (Masalimo 5:4)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 8
ELIYA NDI AHABU
1 Mafumu 16- 17

1.Kodi ufumu wa Israeli unakhalapo ndi mfumu yabwino?
Ayi, onse anali ochimwa. (1 Mafumu 16:30,33; onaninso 2 Mafumu 8:18; 16:3)

2.Kodi ndi mfumu iti yomwe inali yochimwa kwambiri?
Mfumu Ahabu, yemwe anakwatira mkazi oipa wotchedwa Jezebeli. (1 Mafumu 16:30-31)

3.Kodi Ahabu anafuna kuti Israeli atumikire Mulungu?
Ayi, anawauza iwo kuti azitumikira Baala. (1 Mafumu 16:32)

4.Kodi Ahabu anawapanga bwanji anthu kuti azilambira Baala?
Anapha anthu onse amene analambira Mulungu. (1 Mafumu 16:33; 18:3-4)

5.Ndi mneneri wanji anafika kwa Ahabu?
Mneneri Eliya. (1 Mafumu 17:1)

6.Kodi Eliya anamuuza chiani Ahabu?
Anamuuza kuti mvula siibwera kwa zaka zitatu ndi theka. (1 Mafumu 17:1; onaninso Yakobo 5:17)

7.Kodi Eliya anapita kuti nthawi ya chilalayi?
Anapita kukabisala ku Mtsinje wa Keriti. (1 Mafumu 17:2-3)

8.Kodi Mulungu anamudyetsa bwanji Eliya ku mtsinje wa Keriti?
Analamulira makungubwi kumudyetsa iye chakudya. (1 Mafumu 17:4-7)

9.Kodi Mulungu analamulira Eliya kupita kuti pamene mtsinje unauma?
Analamulira iye kupita ku nyumba kwa mkazi wa masiye wa ku Sidoni. (1 Mafumu 17:8-12)

10.Kodi Mulungu anasamalira bwanji Eliya ndi Mkazi wa masiye?
Anawapatsa mafuta ndi chakudya tsiku ndi tsiku. (1 Mafumu 17:13-16)

VESI LOLOWEZA:
"Koma Mulungu wanga adzakwaniritsa chosowa chanu chiri chonse monga mwa chuma chache m'ulemerero mwa Kristu Yesu. (Afilipi 4:19)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 9
ELIYA PA KALIMELI
1 Mafumu 18

1.Kodi chilala chinatha liti?
Pamene Mulungu anamutuma Eliya kwa Ahabu kachiwiri. (1 Mafumu 18:1)

2.Kodi Eliya anamuuza Ahabu kuti apange chiani?
Kuwabweretsa a Israeli onse ku Phiri la Kalimeli. (1 Mafumu 18:17-19)

3.Kodi anabweranso ku Phiri la Kalimeli ndi ndani?
Aneneri a Baala mazana anayi ndi mphambu makumi asanu (450). (1 Mafumu 18:19,22)

4.Kodi Eliya anawauza iwo kuti achite chiani?
Kuti apereke nsembe kwa Baala. (1 Mafumu 18:22-24)

5.Kodi aneneri a Baala anayatsa moto pa guwa lawo?
Ayi, anayenera kufunsa Baala kuti anyeketse ndi moto. (1 Mafumu 18:25)

6.Kodi Baala anatha kutumiza moto?
Ayi, chinali chifano chabe. (1 Mafumu 18:26-29)

7.Chinachitika ndi chiani pamene Eliya anapemphera?
Mulungu anatumiza moto kuchokera kumwamba pa guwa lake. (1 Mafumu 18:30-39)

8.Kodi anthu anafuula kuti chiani pamene anaona zoterezi?
"Yehova ndiye Mulungu" (1 Mafumu 18:39)

9.Kodi Eliya anachita chiani ndi aneneri a Baala?
Anawapha iwo onse. (1 Mafumu 18:40)

10.Chinachitika ndichiani aneneri a Baala ataphedwa?
Mulungu anatumiza mvula kuyankha pemphero la Eliya. (1 Mafumu 18:41-45)

VESI LOLOWEZA:
Ine ndiri Yehova, ndipo palibe winanso; popanda Ine palibe Mulungu"(Yesaya 45:5)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 10
YEHOSAFATI MFUMU YA AYUDA
2 Mbiri 17-20

1.Kodi ufumu wa Yuda unatumikira ana ang'ombe a golide?
Ayi, anapemphera m'kachisi ku Yerusalemu. (2 Mbiri 17:1-4)

2.Tikudziwa chiani zokhuza mafumu a Yuda?
Onse anali a fuko la Davide. (2 Mbiri 32:32-33; 34:1-3; Yeremia 17:25)

3.N'chifukwa chiani Mulungu anaika ana a Davide pa mpando wa chifumu?
Chifukwa Ambuye Yesu anayenera kubadwira ku fuko la Davide. (Mateyu 1:1; onaninso monga Mateyu 9:27)

4.Kodi mafumu onse a Yuda anatumikira Mulungu?
Ena mwa iwo anatha kutero, koma ambiri anali ochimwa. (Monga 2 Mbiri 21:3 -4, 6)

5.Tchulani mfumu yomwe inali yoopa Mulungu atachoka mfumu Rehoboamu?
Yehosafati. (2 Mbiri 17:1 -6)

6.Kodi Yehosafati anawachitira chiani anthu a ku Yuda?
Anawaphunzitsa iwo kutumikira Mulungu. (2 Mbiri 17:7-9)

7.Kodi Yehosafati anachita tchimo lotani?
Anapita pamodzi ndi Ahabu ku nkhondo. (2 Mbiri 18:1-3, 28; 19:2)

8.Chinachitika ndi chiani ku nkhondo?
Ahabu anaphedwa. (2 Mbiri 18:33-34)

9.Kodi Mulungu anamudalitsa bwanji Yehosafati?
Mulungu adamudalitsa ndi chuma chambiri. (2 Mbiri 20:25; 17:3-6)

10.Kodi Mulungu anamuthandiza Yehosafati kumutetezera kwa adani ake?
Inde, Mulungu anapangitsa adani kuti amuope. (2 Mbiri 20:29-30)

VESI LOLOWEZA:
"Yamikani Yehova, pakuti chifundo chache chikhala chosatha"(2 Mbiri 20:21)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 11
MNENERI ELISA
2 Mafumu 2-5

1.Kodi Eliya anafa?
Ayi, Mulungu anamutenga kunka naye kumwamba. (2 Mafumu 2:1)

2.Kodi Mulungu anamutenga iye motani popita kumwamba?
Pa gareta la moto ndi kabvulumvulu. (2 Mafumu 2:11)

3.Ndi mneneri wanji amene analowa m'malo mwa Eliya?
Kapolo wa Eliya, Elisa. (2 Mafumu 2:8-9; onaninso v 12-15)

4.Kodi ana ena anamunyoza bwanji Elisa?
Anafuula nati, "Takwera wadazi" (2 Mafumu 2:23)

5.Kodi Mulungu anawalanga bwanji anyamata amenewa?
Zimbalangondo ziwiri zinapha ana makumi anai ndi mphambu ziwiri (42) (2 Mafumu 2:24)

6.Kodi anabwera kwa Elisa kufuna kuchiritsidwa adali ndani?
Namani wa khate wochokera kwa Aramu (Syria). (2 Mafumu 5:1, 9)

7.Kodi Namani anadziwa bwanji za Elisa?
Mtsungwana wachiyuda wochokera ku Israeli ndi amene adamudziwitsa. (2 Mafumu 5:2-4)

8.Kodi Namani anachiritsidwa bwanji?
Anamvera Elisa ndipo anakasamba kasanu ndi kawiri mu mtsinje wa Yorodani. (2 Mafumu 5:10-11 , 13-15)

9.Kodi ndi tchimo lanji lomwe kapolo wa Elisa anapanga?
Analandira iye matalente (mphatso) kuchokera kwa Namani ngati malipiro (2 Mafumu 5:15-16,20-24)

10.Kodi Kapolo wa Elisa analangidwa bwanji?
Anasanduka munthu wa khate. (2 Mafumu 5:25-27)

VESI LOLOWEZA:
"Ali kuti Yehova Mulungu wa Eliya?" (2 Mafumu 2:14)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 12
ELISA ALONJEZA CHAKUDYA KWA ISRAELI
2 Mafumu 6-7

1.N'chifukwa chiani Mulungu anatumiza mneneri Elisa kwa a Israeli ochimwa aja?
Chifukwa Mulungu anali ndi anthu kumeneko. (2 Mafumu 6:8-10; onaninso 1 Mafumu 19:18)

2.N'chifukwa chiani mfumu ya a Aramu anafuna kumugwira Elisa?
Chifukwa Elisa anathandiza mfumu ya Israeli. (2 Mafumu 6:13-14)

3.Chinachitika ndi chiani ndi asilikali amene anabwera kudzatenga Elisa?
Mulungu anawapangitsa khungu. (2 Mafumu 6:18)

4.Kodi a Aramu analimbananso ndi a Israeli?
Inde, asilikali anamanga misasa yao kuzungulira Samaria. (2 Mafumu 6:24)

5.Kodi izi zinasowetsa bwanji mtendere anthu okhala m'mudzi muja?
Anasowa chakudya. (2 Mafumu 6:25)

6.Kodi iwo anavutika ndi njala?
Inde, mpaka zinafika poti amayi awiri anadya mwana wao. (2 Mafumu 6:26-30)

7.Kodi Elisa analonjeza chiani mfumu?
Kudzakhala chakudya tsiku lotsatiralo. (2 Mafumu 7:1)

8.Kodi mfumu inakhulupirira Elisa?
Ayi, iye ndi anyamata ake anamunyoza Elisa. (2 Mafumu 7:2)

9.Kodi Mulungu anapereka bwanji chakudya ku Samaria?
Mulungu anapangitsa a Aramu kuthawa m'misasa yao. (2 Mafumu 7:5-7, 14-16)

10.Chinachitika kwa mnyamata uja anamunyoza Elisa ndi chiani?
Anaponderezedwa ndipo anafa. (2 Mafumu 7:2,17-20)

VESI LOLOWEZA:
"Ine, Inetu ndine Yehova; ndipo palibe Mpulumutsi, koma Ine ndekha" (Yesaya 43:11)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 13
YEHU MFUMU YA ISRAELI
2 Mafumu 9-10

1.Kodi Elisa analamulira mwana wa mneneri uti kuti amudzoze ngati mfumu ya Israeli?
Yehu, mtsogoleri wa nkhondo. (2 Mafumu 9:2-3)

2.Kodi Yehu analamulidwa kuti achite chiani?
Kuti aphe banja lonse la Ahabu. (2 Mafumu 9:6-10)

3.N'chifukwa chiani Mulungu analamulira iye kuti apange zimenezi?
Chifukwa banja la Ahabu linali lochimwa kwambiri. (2 Mafumu 9:7)

4.Kodi Yehu anapha ndani koyamba?
Mfumu ya Israeli ndi mfumu ya Yuda. (2 Mafumu 9:21, 24, 27)

5.Kodi Mulungu anasangala zoti Yehu anapha mfumu ya Yuda?
Ayi, anauzidwa kuti akaphe a pa banja pa Ahabu okha. (Hoseya 1:4)

6.Kodi Yehu anaphanso Yezebeli?
Inde, anauza anyamata ake kuti amutayire pa zenera. (2 Mafumu 9:30-33)

7.Chinachitika ndi chiani ndi thupi la Yezebeli?
Linadibwa ndi agaru. (2 Mafumu 9:35-37)

8.Kodi banja la Ahabu lonse linaphedwa?
Inde, ana ake amuna makumi asanu ndi awiri (70) onse anadulidwa mitu.
(2 Mafumu 10:6-8)

9.Kodi Yehu ananama bwanji potumikira Mulungu?
Anapha onse amatumikira a Baala. (2 Mafumu 10:18-28)

10.Kodi Yehu anatumikiradi Mulungu?
Ayi, anawayambitsa a Israeli kutumikira mafano. (2 Mafumu 10:29, 31)

VESI LOLOWEZA:
"Nsembe ya oipa inyansa Yehova. (Miyambo 15:8)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 14
MNENERI YONA
Buku la Yona

1.Kodi Mulungu anamuuza chiani Yona?
"Nyamuka, pita ku Nineve, mudzi waukuruwo, nulalikire motsutsana nao" (Yona 1:2)

2.Kodi Yona anapita ku Nineve?
Ayi, anathawa. (Yona 1:3)

3.Chianachitika ndi chiani pamene Yona anali mu ngalawa?
Mulungu anatumiza namondwe pa nyanja. (Yona 1:4-5)

4.Kodi amalinyero anachita naye chiani Yona?
Anam'ponyera pa nyanja. (Yona 1:9-12, 15)

5.Kodi Yona anamira?
Ayi, Mulungu anakonzeratu chinsomba chachikulu kuti chim'meze iye. (Yona 1:17; onaninso Mt 12:40)

6.Kodi iye anafa mmimba mwa chinsomba chija?
Ayi, patatha masiku atatu chinamusanzira ku mtunda. (Yona 1:17; 2:10)

7.Kodi Yona anamvera Mulungu zitachitika zimenezi?
Inde, iye anapita ku Nineve kukawalangiza anthu kuti alape apo ayi Mulungu awaononga. (Yona 3:2-4)

8.Kodi Nineve anawonongedwa?
Ayi, chifukwa anthu ambiri analapa. (Yona 3:5, 10; onaninso Mt 12:41)

9.Kodi Yona anakondwera kamba koti Nineve sanaonongedwe?
Ayi, anakwiya kwambiri. (Yona 4:1)

10.Kodi Mulungu anamuuza chiani Yona pomuchenjeza chifukwa cha kukwiya kwake?
Kuti pali anthu ambiri omwe anali asanamve chilungamo cha Mulungu m'mudzi muja. (Yona 4:11)

VESI LOLOWEZA:
"Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo ine ndizizindikira, ndipo zinditsata ine"(Yohane 10:27)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 15
YOASI MFUMU YA AYUDA
2 Mbiri 22-24

1.Kodi Ataliya anali ndani?
Anali mwana wa mkazi wa mfumu yochimwa Ahabu. (2 Mbiri 22:1-2; 2 Mafumu 8:16-18)

2.Kodi Ataliya anakhala bwanji mfumukazi?
Iye anapha zizukulu zake zonse . (2 Mbiri 22:10)

3.Kodi Ataliya anatha kupha onse?
Ayi, koma mwana Yoasi anabisidwa m'kachisi. (2 Mbiri 22:11-12)

4.Kodi Yoasi anakhala liti mfumu?
Pamene anali ndi zaka zisanu ndi ziwiri (7) za kubadwa. (2 Mbiri 23:1; 24:1)

5.Kodi anathandizira kuti Yoasi akhale mfumu adali ndani?
Yehoyada,wansembe owopa Mulungu. (2 Mbiri 23:1-3,11)

6.Chinamuchitikira ndi chiani Ataliya?
Anaphedwa. (2 Mbiri 23:21 mpaka kutsogolo)

7.Kodi Yoasi anakhulupirika?
Inde, anachita ichi masiku onse a Yehoyada wansembe anali moyo. (2 Mbiri 24:2)

8.Kodi chabwino chimene Yoasi anachita ndi chotani?
Iye anakonzanso nyumba ya Yehova. (2 Mbiri 24:4-5,11-14)

9.Kodi Yoasi anachita chiani wa nsembe atafa?
Anayamba kutumikira mafano. (2 Mbiri 24:17-18)

10.Kodi Yoasi anachitanso tchimo lanji?
Anapha mwana wa Yehoida yemwe anali mneneri. (2 Mbiri 24:20-22)

VESI LOLOWEZA:
"Iye amene akhala pansi m'ngaka yache ya Wam'mwambamwamba;Adzagonera mu mthunzi wa Wamphamvu yonse"(Masalimo 91:1)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 16
HEZEKIYA MFUMU YA AYUDA
2 Mafumu 16-20 ndi 2 Mbiri 29-32

1.Tchulani mfumu ina yabwino ya Ayuda.
Hezekiya, m'modzi mwa mfumu yoopa Mulungu ku Yuda. (2 Mafumu 18:1-7; 2 Mbiri 32:32-33)

2.Kodi anthu anali akutumikirabe Mulungu pamene Hezekiya amapatsidwa ufumu?
Ayi, ngakhale nyumba za Yehova anatseka makomo awo. (2 Mafumu 16:8, 14, 18; 2 Mbiri 28:24; 29:6-7)

3.Kodi Hezekiya anafuna anthu adzitumikira Mulungu?
Inde, anatsegula makomo omwe anatsekedwa a nyumba ya Mulungu. (2 Mbiri 29:3)

4.Kodi Hezekiya anachita chiani ndi mafano?
Anaononga zonse. (2 Mafumu 18:4)

5.Kodi Hezekiya anaononganso malo a pa mwamba omwe amagwiritsa ntchito popembezera Mulungu?
Inde, Pakuti Mulungu yekha ndiye akhoza kupembezedwa monga mmene Iye analamulira. (2 Mafumu 18:4, 22; onaninso Deutronomo 12:32)

6.Kodi Hezekiya anaonetsanso chiani pofuna kuti anthu a Yuda adzitumikira Mulungu?
Anachita phwando lalikulu la paskha. (2 Mbiri 30:1)

7.Kodi Hezekiya anaitana anthu a ku Yuda okha ku phwando kuja?
Ayi, anaitananso anthu a ku Israeli kumpoto kwake. (2 Mbiri 30:1-2)

8.Kodi anthu a ku Israeli anabwera Hezekiya atawaitana?
Inde, ambiri anabwera koma ambiri a iwo anakana. (2 Mbiri 30:10-13)

9.Chinachitika ndi ufumu wa Israeli ndi chiani nthawi yomwe Hezekiya anali mfumu?
Mulungu anawatengera iwo ku ukapolo chifukwa cha machimo awo. (2 Maf 18:10-11; 17:5-6)

10.Kodi anthu a ku Israeli (amenewa ndi mafuko khumi a kumpoto) anabwereranso kwao?
Ayi, ambiri a iwo sanabwerere. (onani Machitidwe 2:5-11)

VESI LOLOWEZA:
"Wodalitsika mtundu wa anthu umene Yehova ndiye Mulungu wao" (Masalimo 33:12)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 17
HEZEKIYA ADWALA
Yesaya 36-39

1.Ndani anabwera kudzamenyana ndi Hezekiya?
Mfumu ya Asuri ndi a nkhondo ake. (Yesaya 36:1)

2.Kodi mfumu ya Asuri inachita chiani?
Anatuma kazembe kukawakhumudwitsa ndipo anatumiza kalata kwa Hezekiya. (Yesaya 36:4-7, 13-18; 37:8-14)

3.Kodi kalatayo inanena chiani?
Mulungu amene akumtumikirayo sangamuthandize Hezekiya. (Yesaya 37:10)

4.Kodi Hezekiya anachita chiani ndi kalata ija?
Anakwera kunka ku nyumba ya Mulungu ndipo anapemphera. (Yesaya 37:14-15)

5.Kodi Yesaya anamuuza Hezekiya kuti achite chiani?
Kuti akhulupirire Mulungu yekha. (Yesaya 37:5-6; 2 Mafumu 19:20-21,32-34)

6.Kodi Mulungu anathandiza bwanji Hezekiya ?
Anaononga asilikali a Asuri. (Yesaya 37:36)

7.Chinachitika kwa Hezekiya nthawi imeneyi ndi chiani?
Anadwala kwambiri. (Yesaya 38:1)

8.Kodi Hezekiya anapemphera chiani mu pemphero lake?
Anapemphera kuti achiritsidwe. (Yesaya 38:2-3)

9.Kodi Mulungu anayankha pemphero lake?
Inde, Mulungu anamuchiza ndipo anampatsa mwana wa mwamuna. (Yesaya 38: 4-5; 2 Mafumu 20:21)

10.Kodi mwanayu anali ndani?
Manase. (2 Mafumu 20:21-21:1)

VESI LOLOWEZA:
'Yehova ndiye kuunika kwanga ndi chipulumutso changa; ndidzaopa yani?'(Masalimo 27:1)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 18
MANASE MFUMU YA AYUDA
2 Mbiri 33

1.Anakhala mfumu atachoka Hezekiya ndi ndani?
Mwana wake Manase. (2 Mbiri 33:1)

2.Kodi Manase anali mfumu yabwino?
Ayi, anali oipa kwambiri. (2 Mbiri 33:2-5)

3.Kodi ndi choipa chanji chimene Manase anachita?
Anapereka ana ake ku mafano. (2 Mbiri 33:6)

4.Kodi Manase anachitanso tchimo lanji potsutsana ndi Mulungu?
Anapha anthu a Mulungu. (2 Mafumu 21:16)

5.Kodi Mulungu anamulanga bwanji Manase?
Anamuika mndende ku Babulo. (2 Mbiri 33:11)

6.Kodi Mulungu anachita naye chiani Manase mu ndende?
Mulungu anampangitsa iye kudzichepetsa ndi kulapa machimo ake. (2 Mbiri 33:12)

7.Kodi Manase anakhalitsa mu ndende?
Ayi, anakhalanso mfumu. (2 Mbiri 33:13)

8.Kodi Manase anasonyeza bwanji kuti analapa machimo ake?
Anachotsa mafano onse m'nyumba ya Mulungu. (2 Mbiri 33:15)

9.Kodi Manase anabwezeretsanso kupembeza kwa Mulungu?
Inde, ansembe anayambanso kupereka nsembe kwa Mulungu. (2 Mbiri 33:16)

10.Kodi anthu analapadi?
Ayi, mokhumudwitsa, anabwereranso ku machimo ao. (2 Mbiri 33:17)

VESI LOLOWEZA:
"Chifukwa cha dzina lanu, Yehova, Ndikhululikireni kusakaza kwanga, pakuti ndiko kwakukuru" (Masalimo 25:11)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 19
YOSIYA MFUMU YA AYUDA
2 Mafumu 22-23

1.Kodi mfumu yotsiriza yabwino ya Yuda ndi ndani?
Yosiya. (2 Mafumu 22:1-2; 23:25)

2.Kodi Yosiya anaonetsa bwanji kuti iye amaopa Mulungu?
Anaphwanya mafano onse. (2 Mafumu 23:6,24; 2 Mbiri 34:3-4)

3.Kodi Yosiya anakonzanso kachisi?
Inde, anatuma amuna kukonza kachisi. (2 Mafumu 22:3-6)

4.Kodi Hilikiya wansembe wamkulu anapeza chiani m'kachisi?
Buku la chilamulo. (2 Mafumu 22:8; onaninso 2 Mbiri 34:14-15)

5.Kodi mfumu anapanga chiani ndi malamulo?
Anawerenga kwa anthu. (2 Mafumu 23:1-2)

6.Kodi Yosiya anawauza anthu kuti achite chiani?
Ayenera kupitiriza kuchita paska. (2 Mafumu 23:21)

7.Kodi phwando limene anthu anachita linali lalikulu?
Inde, kwa zaka zambiri panalibenso phwando lalikulu ngati limeneli? (2 mafumu 23:22-23)

8.Kodi Yosiya anafa bwanji?
Anaphedwa ku nkhondo. (2 Mafumu 23:29-30; 2 Mbiri 35:20-24)

9.Kodi anthu anapitiriza kutumikira Mulungu?
Ayi, anachita zoipa zambiri. (2 Mbiri 36:14-16)

10.Kodi Mulungu anawachenjeza chiani anthu aja?
Adzalanga Ayuda monga m'mene analagira a Israeli. (2 Mafumu 23:26-27)

VESI LOLOWEZA:
"Mau anu ndiwo nyali ya kumapazi anga,Ndi kuunika kwa panjira panga" (Masalimo 119:105)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 20
MNENERI YEREMIYA
Yeremiya 1, 25, 37 -39 ndi 43

1.Kodi Yeremiya ndi ndani?
Anali mneneri wa ku Yuda. (Yeremiya 1:1; 4-5)

2.Kodi Mulungu anaitana liti Yeremiya kuti akhale mneneri?
Pamene iye anali mnyamata. (Yeremiya 1:6-7)

3.Kodi Yeremiya ananena chiani zokhuza Yerusalemu?
Zoti Yerusalemu adzatenthedwa moto. (Yeremiya 37:6-11)

4.Kodi Yeremiya ananena kuti chidzachika chiani kwa anthu?
Anawauza kuti adzatengedwa kupita ku Babulo. (Yeremiya 37:17; 38:2-3)

5.Kodi mfumu ndi ansembe anakhulupirira Yeremiya?
Ayi, anamukwiyira kwambiri. (Yeremiya 38:4-5)

6.Kodi Jeremiya anazunzika motani?
Anaponyedwa mu dzenje. (Yeremiya 38:6)

7.Kodi Mulungu anawalanga anthu monga mmene ananenera?
Inde, anawatengera ku Babulo. (Yeremiya 39:6-9)

8.Kodi Yeremiya anapita nao?
Ayi, iye ndi anthu ena anatsala ku Yerusalemu. (Yeremiya 39:11-14)

9.Kodi Yeremiya anakhala mu Yerusalemu?
Ayi,anthu anamutenga iye napita naye naye ku Aigupto. (Yeremiya 43:4-7)

10.Kodi Yeremiya anawalonjeza chiani anthu anatengedwa ukapolo?
Patatha zaka makumi asanu ndi awiri (70), Mulungu adzabwezera anthu ku dziko lao. (Yeremiya 25:11)

VESI LOLOWEZA:
"Chifukwa chakusathedwa ife ndicho chifundo cha Yehova, pakuti chisoni chake sichileka" (Maliro 3:22)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 21
DANIELI NDI ANZAKE
Danieli 1-4

1.Kodi anatengedwa pamodzi ndi Ayuda kupita nawo ku Babulo ndi ndani?
Danieli ndi anzache atatu. (Danieli 1:1-4, 6-7)

2.Chinawachitikira ndi chiani Danieli ndi anzache aja?
Anawakweza kuti aziyang'anira dera lonse la Babulo. (Danieli 3:30; 2:48-49; 6:1-3)

3.Kodi Mulungu anawonetsa bwanji kuti ali ndi iwo?
Anawapatsa nzeru zapamwamba kuposa wina aliyense ku Babulo kuja. (Danieli 1:17-20)

4.Kodi Danieli anaonetsa bwanji nzeru zimenezi?
Anamasulira loto la Nebukadinezala. (Danieli 2:1, 19, 28-29, 47)

5.Kodi loto la Nebukadinezala linali lotani?
Linali loti fano lalikuli linaonongedwa ndi mwala. (Danieli 2:31-35)

6.Kodi lotoli limatanthauza chiani?
Khristu adzaononga maiko onse oipa a padziko lapansi. (Danieli 2:35-46; onaninso Masalimo 2:9; Masalimo 110; 1 Akorinto 15:24-25; Chivumbulutso 17:12-18)

7.Kodi abwezi atatuwa anapembeza Mulungu ku Babulo kuja?
Inde, iwo sanapembeze mafano a mfumu aja. (Danieli 3:4-5, 8-18)

8.Kodi Mfumu inawalanga chifukwa cha chimenechi?
Inde, anawaponyera iwo mu ng'anjo ya moto. (Danieli 3:19-23)

9.Kodi iwo anapsa mu ng'anjo muja?
Ayi, Mulungu anawatumizira mmodzi yemwe amaoneka "ngati Mwana wa Mulungu" (Danieli 3:25) mu ng'anjo ndi iwo. (Danieli 3:24-27)

10.Kodi mfumu ija inalangidwa bwanji chifukwa chodzikweza?
Mulungu anamuuza iye kuti adzakhala ngati nyama. (Danieli 4:23-33)

VESI LOLOWEZA:
"Taonani Mulungu wathu amene tintumikira akhoza kutilanditsa m'ng'anjo yotentha ya moto, nadzatilanditsa m'dzina lanu mfumu" (Danieli 3:17)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 22
DANIELI MU DZENJE LA MIKANGO
Danieli 6

1.Kodi Danieli amapemphera kwa Mulungu ku Babulo?
Inde,amapemphera poyang'ana ku Yerusalemu katatu pa tsiku. (Danieli 6:10)

2.N'chifukwa chiani Danieli anapemphera poyang'ana ku Yerusalemu?
Chifukwa Yerusalemu imaimirira chikhulupiriro cha Mulungu ndikupezeka kwake. (Onaninso Masalimo 48:1-3; 132:13; Yesaya 2:2-3)

3.Kodi akalonga anzake a Danieli aja anachita naye nsanje?
Inde, ndipo anafuna kumupha iye. (Danieli 6:3-5)

4.Kodi anafuna kumupha bwanji?
Anafunsa mfumu kuti ikhazikitse lamulo lachifumu ndikuikapo choletsa cholimba. (Danieli 6:6-7)

5.Kodi lamulo la choletsalo ndi lotani?
Loti anthu onse ayenera kugwadira mfumu. (Danieli 6:8-9)

6.Kodi Danieli anamvera mfumu?
Ayi,anapemphera kwa Mulungu monga mmene amachitira kale. (Danieli 6:10)

7.Kodi mfumu inachita chiani ndi Danieli kamba kokana kum'gwadira iye?
Anam'ponyera iye mu dzenje la mikango. (Danieli 6:12-17)

8.Kodi mikango ija inamudya?
Ayi, Mulungu anaitseka pakamwa pa mikango. (Danieli 6:20-22)

9.Kodi mfumu inachita nao chiani akalonga oipa aja?
Anawaponyera iwo mu dzenje la mikango. (Danieli 6:24)

10.Kodi mikango ija inawadya?
Inde, inawalandilira asanafike pansi. (Danieli 6:24)

VESI LOLOWEZA:
"Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu" (Machitidwe 5:29)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 23
KUBWERERA KUCHOKERA KU BABULO
Ezra 1-6

1.Kodi Ayuda anakhala ku Babulo nthawi yaitali bwanji?
Pafufupi zaka makumi asanu ndi awiri (70) (Danieli 9:2)

2.Kodi anabwerera bwanji?
Mulungu anauza mfumu Koresi ya ku Perisiya kuti atsogolele Ayuda ulendo obwerera. (Ezra 1:1-4)

3.Ndi angati anabwerera ku Yerusalemu?
Pafupifupi anthu okwana 50,0000 (Ezra 2:64-65)

4.Kodi choyamba chimene anthu anachita ndi chiani?
Anamanga guwa la nsembe ndipo anapembeza Mulungu. (Ezra 3:1-3)

5.Kodi anthu anachita chiani atamanga guwa la nsembe?
Anayamba kumanga kachisi. (Ezra 3:7-9)

6.Kodi anamaliza kumanganso kachisi uja?
Inde, koma patatha zaka zopitirira makumi awiri (20) polimbikitsidwa ndi mneneri Haggai ndi Zakaliya. (Ezra 5:1-2; 6:14-15)

7.Kodi anthu anasangalala pamene anayambanso kugwiritsa ntchito kachisi?
Inde, koma ena analira. (Ezra 3:12-13)

8.Ndichifukwa chiani ena analira?
Chifukwa kachisi wa Solomoni anali okongola koposa. (Ezra 3:12; Haggai 2:3)

9.Anazunza Ayuda ndani?
Asamariya oipa. (Ezra 4:1-10)

10.Anawazunza bwanji Ayuda?
Anafuna kuwaletsa kumanga kachisi. (Ezra 4:3-5)

VESI LOLOWEZA:
"Yehova anatichitira ife zazikulu;potero tikhala okondwera" (Masalimo 126:3)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 24
ESTERE
Buku la Estere

1.Kodi Ayuda onse anabwerera ku Yerusalemu?
Ayi, ena anatsala ku Babulo. (Estere 2:5-6; 3:6)

2.Tchulani anthu awiri omwe anatsala?
Moredekai ndi Estere mwana wa mkazi wa atate wamng'ono. (Estere 2:5-7)

3.Chinachitika ndi Estere kumeko ndi chiani?
Anakhala mkazi wamkulu wa mfumu. (Estere 2:2-4, 8-9, 16-17)

4.Kodi yemwe anali wankulu wa akalonga onse ndi ndani?
Hamani yemwe anamuda Moredikai. (Estere 3:1-2, 5)

5.Kodi Hamani anafuna kuchita chiani?
Anafuna kupha Ayuda onse. (Estere 3:6, 8-12)

6.Kodi anamva za chiwembu chimenechi ndani?
Moredikai, yemwe anamuuza Estere pozera mwa Hataki mdindo wa mfumu. (Estere 4:1-10)

7.Kodi Estere anamuuza mfumu?
Inde, anamuuza pamene anali pa phwando. (Estere 6:14 - 7:7)

8.Kodi Ayuda onse anaphedwa?
Ayi, mfumu inawauza iwo kuti adzitetedze. (Estere 8:7-11)

9.Chinachitika ndi chiani kwa Hamani?
Anapachikidwa pa mtengo womwe adaukonzera Moredikai. (Estere 7:9-10)

10.Ichi chisonyeza chiani?
Mulungu amasamalira anthu ake nthawi zonse. (Estere 8:1, 15-17; 9:1-5; Yeremia 24:6-7)

VESI LOLOWEZA:
"Thandizo lathu liri m'dzanja la Yehova,Wolenga kumwamba ndi dziko lapansi" (Masalimo 124:8)

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 25
NEHEMIYA
Buku la Nehemiya

1.Kodi Nehemiya anali ndani?
Anali wothirira mfumu chakumwa. (Nehemiya 1:1a, 11)

2.Kodi Nehemiya anamva chiani za Ayuda?
Anamva zoti anasiya kumanga makoma a Yerusalemu. (Nehemiya 1:1-3)

3.Kodi Nehemiya anachita chiani atamva izi?
Anapempha mfumu kuti amulore apite ku Yerusalemu. (Nehemiya 2:1-5)

4.Kodi Nehemiya anachita chiani atafika ku Yerusalemu?
Anauka usiku nazonda makomawo. (Nehemiya 2:12-13)

5.Kodi Nehemiya anafikira kumanga linga lija?
Inde, anawauza anthu kuti ayambe kugwira ntchito. (Nehemiya 2:17-18; 3:1-32; 4:6)

6.Kodi anthu ananyozedwa bwanji?
Anthu oipa anafuna kuimitsa ntchito ija. (Nehemiya 2:19; 4:1-3, 7-8)

7.Kodi anasiya kugwira ntchito ija?
Ayi, Nehemiya anawapatsa malupanga anthu onse. (Nehemiya 4:13-18)

8.Kodi anthu oipawa aja anapitirizabe kuwavutitsa?
Inde,anamunenera zonama Nehemiya? (Nehemiya 6:5-8, 12-14)

9.Kodi anthu anatenga nthawi yaitali bwanji kumanga linga?
Anamanga masiku makumi asanu ndi mphambu awiri (52) (Nehemiya 6:15)

10.Kodi linga linamangidwa mofulumila bwanji?
Mulungu anawathandizira anthu ake kumanga. (Nehemiya 2:19-20; 4:16-23; Ezra 9:8-9)

VESI LOLOWEZA:
"Yehova wa makamu, Wodala munthu wa kukhulupirira Inu" (Masalimo 84:12)

Copyright © Gratia Dei Sola Media